# UNDUNA WA ZACHILENGEDWE NDI KUSINTHA KWA NYENGO


## NTHAMBI YOONA ZA NYENGO NDI KUSINTHA KWA NYENGO

### ULOSI WA KAGWEDWE KA MVULA M'BOMA LA NTCHISI M'DZINJA LA 2024-2025

## DZINJA LA 2024/2025 MWACHIDULE


Nyengo ya dzinja ya 2024/2025 ikuyembekezereka kukhudzidwa ndi La Nina wochepa mphamvu. La Nina ndi kuzizira kwa madzi mdera la pakati chakum'mawa kwa nyanja yamchere ya Pacific. Izi zikhala chomwechi mpaka kumayambiriro a chaka cha 2025.
Boma la Ntchisi likuyembekezera kulandira mvula ya mlingo wokhazikika, komanso oposerapo koma pali kuthekera kolandira mvula yochulukirapo m'mwezi wa February 2025 kuposa mwezi wa February chaka chatha.

## October 2024





Mweziwu, Madera ambiri kudzakhala kopanda mvula koma m'madera ena a m'boma la Ntchisi akuyembekezera kulandila mvula yochepera mlingo wa 50 mm.
Mvulayi idzakhala ndi mphepo ya mkuntho m'madera ena.

## November 2024





Mweziwu, Madera ambiri kudzakhala kopanda mvula koma m'madera ena a m'boma la Ntchisi akuyembekezera kulandira mvula yochepera mlingo wa 50 mm.
Mvulayi idzakhala ndi mphepo ya mkuntho ndi ziphaliwali m'madera ena

## December 2024





Madera ambiri ayembekezere mlingo wa mvula wa pakati pa 100-180mm. Komabe madera ena ozungulira SC Nthondo ndi ku mpoto cha kuzambwe kwa TA Kasakula ayembekezere mvula ya mlingo wokwana 250mm. Mvula yodzalira idzayamba kugwa sabata yachitatu ndi sabata yachinayi ya mwezi wa December, koma madera ena akhoza kulandira mvula mofulumirako.

## January 2025





Mwezi wa January ukuyembekezereka kukhala mwezi wachinyontho ndipo madera ambiri adzalandila mvula ya mlingo wa pakati pa 200 ndi 300 mm omwe ndi mlingo wake wamvula wokhazikika ndi kupyolerapo. Madera a SC Chilooko ndi ena a TA Kasakula ayembekezere kulandila mvula ya mlingo opitilira 300mm.
.

## February 2025





Mu February, madera ambiri ayembekezere kulandira mvula ya mlingo wa pakati pa 150-200mm. Komabe madera ena a SC Nthondo, TA Kasakula ndi ku mpoto cha kuzambwe kwa SC Chilooko akhoza kulandira mvula ya mlingo okwana 250mm. Pali chiyembekezo chochuluka cha ng'amba yoposa sabata imodzi mmweziwu.

## March 2025




Madera ambiri mu February ayembekezere mvula ya mlingo okhazikika pamene madera ena ozungulira SC Nthondo ndi ku mpoto cha kumadzulo kwa TA Kasakula atha kulandira mvula yochulukirapo yokwana 260mm.


## April 2025




April ndi mwezi otsiliza wa nyengo ya dzinja ku Malawi, nyengoyi ikuyembekezereka kutha kuyambira sabata yoyamba mpaka sabata lachiwiri la mwezi wa April.
Madera ambiri m'bomali adzalandila mvula ya mlingo ochepela 50mm.

M'boma la Ntchisi Mvula yodzalira idzayamba kugwa sabata yachitatu ndi sabata yachinayi ya mwezi wa December, koma madera ena akhoza kudzalandira mvula mofulumirako. Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kudzatha pakati pa sabata loyamba mpaka sabata lachiwiri la mwezi wa April. Nyengo ya dzinja ikuyembekezereka kukhala masiku a pakati pa 100 ndi 140. Ng'amba yapafupifupi sabata imodzi ikuyemnekezeleka mwezi wa February m'madera ena a m'bomali
Ndondomeko ya kagwedwe ka mvula ku Ntchisi yaperekedwa pansipa;

| NTCHISI AGRICULTURE | | | |
|---|---|---|---|
| MONTH | NORMAL RANGE | | FORECAST |
| OCT | 0 | 1 | 1 |
| NOV | 14 | 41 | 37 |
| DEC | 153 | 205 | 226 |
| JAN | 186 | 281 | 291 |
| FEB | 184 | 249 | 230 |
| MAR | 97 | 178 | 285 |
| APR | 11 | 54 | 41 |




Zasindikizidwa ndi thandizo lochokera ku:

**Ulosiwu udzasindikizidwanso mu mwezi wa December 2024**


**Mukafuna kudziwa zambiri lemberani kwa:**
The Director of Climate Change and Meteorological Services, P.O. Box 1808,Blantyre.
Tel +265 1 82 47 12 / Cell: +265 882 26 65 79 Email: metdept@metmalawi.gov.mw ; Website: www.metmalawi.gov.mw